


Mbusa Tony Alamo — Fuko La Chikhristu La Alamo — Volume 06000



*Mbusa Tony Alamo—chithunzi 1986*

# UMBONI WA TONY ALAMO

## Mafupa Owuma

Yolembedwa ndi
**Tony Alamo**

**Ezekieli, yemwe ndi mneneri wa mu Chipangano Chakale, anaona masomphenya ochokera kwa Mulungu. Iye anaona chigwa cha mafupa owuma, chomwe chinaimira kufa mwa uzimu kwa Isiraeli ndiponso dziko lonse lapansi. Masomphenyawa analosera za kubwera koyamba kwa Khristu, kulalikira kwake uthenga wabwino ndiponso zotsatira zake, kuukitsidwa kwa akufa koyamba n'kulandira moyo wosatha kwa anthu onse amene amakhulupirira "Mawu a Ambuye."[1]**

**Mulungu anamufunsa Ezekieli kuti, "Iwe mwana wa munthu, kodi mafupa amenewa angakhalenso ndi moyo?" (Kodi anthu amene anafa mwauzimu angakhalenso ndi moyo?) Ezekieli anayankha kuti, "Ambuye, mukudziwa ndinu chifukwa ndinuyo amene munawalenga."[2]**

Kenako Mulungu analankhulanso ndi mneneriyu n'kumuuza kuti, "Losera zokhudza mafupawa ndipo ulankhule nawo kuti, mafupa owuma inu, imvani Mawu a Ambuye. Ambuye akulankhula ndi mafupawa kuti: Taonani, ndidzachititsa mpweya kulowanso mwa inu, ndipo mudzakhalanso ndi moyo."[3]

Mtundu wa Isiraeli unkadziwiratu kuti unali utalowerera kotheratu ngati mtundu.[4] Pomafika nthawiyi, Aisiraeli anali atagawanika komanso anali opanda chiyembekezo chilichonse. Koma Mulungu anamuuza Ezekieli kuti Iye adzautsa mtundu wina waukulu kuposa mtundu woyambirira wa Isiraeli, womwe unkapitiriza kuchimwira Mulungu. Mtundu wachiwiri wa Isiraeli udzakhala wa anthu ochokera mumtundu uliwonse padziko lapansi,[5] anthu okhulupirika ochokera mwa Ayuda ena osankhidwa komanso khamu la anthu Amitundu amene anaphatikizidwa ku Mpesa Weniweni (Khristu).[6] Mtunduwu unali kudzakhala waukulu komanso wopatulika, wopangidwa ndi anthu amene anaukitsidwa kwa akufa mu uchimo n'kukhalanso ndi moyo wosatha.[7] Mtundu umenewu sudzakhala wogawanika pamaso pa Mulungu. Uku kunali kuukitsidwa koyamba kudzera mwa mphamvu zoukitsa akufa za Khristu.[8]

Mu 1964, ndisanaukitsidwe koyamba ndi Khristu, ineyo, Bernie Hoffman, amene ndimadziwikanso ndi dzina loti Tony Alamo, ndinali wodziwika bwino kuti ndine munthu wokonda kuchita machimo komanso zinthu zosaopa Mulungu. Sindinkamudziwa Mulungu ngakhale pang'ono. Sindinkadziwa n'komwe zoti kunja kuno kuli Mulungu. Ndinkangoona kuti nkhani zonse zimene zili m'mawu a Mulungu ndi zongopeka komanso nthano, ndipo sindinkamvetsa chifukwa chake anthu ena amakhulupirira Mulungu komanso Mwana Wake. Zinkandivuta kumvetsa kuti n'chifukwa chiyani anthu ena amakhulupirira Mulungu chifukwa anthuwo anali odzikonda. Ndinkaona kuti anthuwo amachitanso machimo ngati ine ndemwe, mwinanso kundiposa. Ndinkadziwa zimenezi chifukwa ena mwa anthuwa ndinkacheza nawo. Tonse tinali akufa, tinali mulu wa mafupa owuma. Ndinkakwiya koopsa wina akayeserera kundiuzako za Chikhristu chifukwa ndinkaona kuwerenga Baibulo n'kungotaya nthawi. M'moyo mwanga ndinalibe nthawi yoseka ndi munthu kapena kumvera zopusa.

Anthu ankaona kuti ndine katswiri pa nkhani za malonda. Ndinathandiza anthu ambiri padziko lapansi kuti alemere komanso atchuke. Ena mwa anthu amene ndinawathandizawa ndi oimba odziwika bwino, anthu ochita masewero ndi makanema, komanso ndinatukula ndi kutsatsa malonda a zipangizo zosiyanasiyana zogwiritsidwa ntchito pakhomo. Koma nditakumana ndi zokhoma kwambiri m'moyo wanga ndi pamene ndinatembenuka mtima ndikuyamba kufalitsa timapepala tonena za Yesu m'misewu, ndinayamba kukhala pamishoni ndikumalalikira uthenga wabwino, komanso ndinayamba kuyendetsa ntchito yosonkhanitsa zakudya n'kumagawira anthu a njala.

Pofika m'zaka za ma 1960, zinali zoonekeratu kuti zinthu zikusokonekera padzikoli. Anthu ambiri anayamba kugwiritsa mankhwala osokoneza bongo, komanso kuchita makhalidwe ambiri oipa. Ndipo ndinkadana ndi zimene *hippie*

*(Yapitilira pa tsamba 2)*

**1** Ezek. 36:1, 4 **2** Ezek. 37:3, ochokera ku Chihe. **3** Ezek. 37:4-5, ochokera ku Chiaramu **4** Ezek. 37:11 **5** Gen. 17:4-16, 22:18, 26:4, 46:3, 48:19, 49:10, Eks. 19:6, 32:10, Sal. 22:27, Yes. 2:2, Yoh. 11:51-52, Mac. 10:34-35, Aef. 1:10, Aheb. 8:8-12, 1 Pet. 2:9-10, Chiv. 5:9, 14:6 ndi ena ambiri **6** Yoh. 15:1, Aro. 11:17, 19, 23, 24, Chiv. 7:4 **7** 1 Pet. 2:9 **8** Aro. 15:12, 1 Akor. 15:15, 16, Akol. 2:12, 3:1, 1 Ates. 4:16, Chiv. 20:5-6,

## UMBONI WA TONY ALAMO

*(Yachokera pa tsamba 1)*

*movement* inkachita ku Hollywood, Sunset komanso padziko lonse lapansi. N'zoona kuti ngakhale ine amene ndinkachitanso zinthu zina zoipa. Sizinkandikhudza ngati anthu akuchita zinthu zoipa, bola ngati ankachita zinthuzo pamalo osaonekera kwa mabanja ndi ana. Kwa ine dziko linali litatha, litafa, litauma, litanyasa kwambiri, ndiponso litayipiratu.[9] Ndinkaona kuti palibe chifukwa chilichonse chokhalira ndi moyo. Ndinkakhulupirira kuti anthu enanso padzikoli akuona chimodzimodzi ngati ine, ndipo ndidayamba kugwiritsanso ntchito mankhwala osokoneza bongo pofuna kuthawa mavuto. Ndinkaona kuti atsogoleri a matchalitchi ndi anthu achinyengo; ndipo aliyense ankatha kuona bwinobwino zimenezi. Dziko lonse linali lakufa ndi uchimo komanso ntchito zake zoipa.[10] Dziko lonse linali ngati chigwa chachikulu cha mafupa owuma, chimene Ezekieli anaona.[11]

Ndili mu ofesi ku Beverly Hills, ndinakumana ndi Yesu m'njira yodabwitsa kwambiri. Palibe amene angamvetse m'mene ndinkaopera komanso pa nthawi yomweyo m'mene ndinasangalalira pamene Mulungu anadzisonyeza kuti Iye ndiponso Mwana wake alipodi. Ndinasangalala kwambiri nditadzadzidwa ndi Mzimu Wake Woyera komanso nditamva mawu Ake amphamvu amene anandikuta thupi langa lonse. Maonekedwe ake anali aulemerero komanso osangalatsa. Ndinadzazidwa kwambiri ndi Mzimu wake Woyera ngati kuti ndagwiridwa ndi dzanja la mphamvu la Mulungu. Kenako ndinamva mawu ake akundiuza kuti: "Imirira ndipo uwuze anthu amene ali m'chipinda chino zokhudza Ambuye Yesu Khristu. Uwawuzenso kuti Iye adzabweranso padzikoli ndipo sadzafanso." Pamene Mzimu wake Woyera unabwera muofesiyo n'kundidzaza, ndinatha kuzindikira kuti Iye ndi wanzeru zodabwitsa.[12] Iye anali paliponse ndi mumpweya momwe. Ankadziwanso chilichonse chimene chinachitikapo m'mbuyomu komanso chimene chidzachitika m'tsogolo.[13] Ndinali wamanyazi chifukwa ndinkadziwa kuti Iye akudziwa chilichonse chimene chinachita pamoyo wanga. Kenako anandisonyeza kuti Kumwamba komanso Gehena zilipodi. Ndinkadziwiratu kumene ndikadapita ndikadapanda kuchita zimene Iye ananena...ndipo sikunali Kumwamba.

Ngakhale kuti ndinkaopa kwambiri,[14] ndinasangalalanso kudziwa kuti Mulungu ndi weniweni ndiponso ndi wamoyo. Iye ali monga m'mene aneneri komanso atumwi anamufotokozera. Iye sanasinthe ngakhale pang'ono kuyambira nthawi imene analenga kumwamba, dziko lapansi, ndiponso zinthu zonse zimene zilimo.[15] Nthawi yomweyo ndinadziwiratu kuti nthawi zonse ndizimuopa, kumulemekeza, kumukonda, ndiponso kumutumikira. Ndinadziwa kuti ndidzafunitsitsa kukhala ndi moyo, kuzunzidwa, ndi kumufera Iye, ndikupanga zonsezi mosangalala, ndi chimwemwe chonse.[16]

Mulungu atandimasula mu ofesiyo, ndinamufunsa kuti, "Kodi Mukufuna kuti ndichite chiyani? Ndichita chilichonse chimene Munganene." Koma sindinayankhidwe, choncho ndinaganiza kuti akufuna ndipite kutchalitchi. Ndinkaganiza kuti tchalitchi chachikulu kwambiri n'chimene chilinso chabwino kwambiri, choncho ndinapita kutchalitchi chachikulucho, koma sindinapeze Mulungu kumeneko. Kenako ndinapita kumatchalitchi ena, koma kumenekonso kunalibe Mulungu. Ndiyeno ndinayamba kuwerenga mabuku okhala ndi zithunzi m'zikuto zake. Zithunzizo zinali za anthu owoneka ngati anzeru komanso opemphera, okhala ndi ndevu zitalizitali komanso ovala zovala zachipembedzo. Koma ndinadziwa kuti zimene zinali m'mabukuwo zinali zolakwika chifukwa zinkasonyeza kuti Mulungu si woyenera kumuopa,[17] zoti Mulungu saopseza anthu, ndiponso zoti munthu angachite tchimo lililonse koma sakawotchedwa ku Gehena.[18] Sikuti ine ndinkafuna Mulungu wotere, koma ndinkafuna kupeza Mulungu amene anandiopseza,[19] Mulungu amene anandionetsa Kumwamba komanso ku Gehena, Mulungu amene anandichititsa kuchita zinthu zomwe sindinachitepo, zomwe sindinkafuna kuchita.

M'mbuyomu, ndinkaganiza kuti chowonadi sichingapezeke mu Baibulo chifukwa pali mabaibulo ambirimbiri. Ndinkakhulupirira kuti chilichonse chimene anthu ambiri angachikhulupirire sichingakhale chanzeru chifukwa ndinkaona kuti anthu onse ndi opusa. Kenako ndinayamba kuwerenga Baibulo ndipo ndinazindikira njira yopezera chipulumutso komanso ndinapeza malangizo opezera moyo wosatha. Malangizowo amafotokozanso m'mene munthu angakulire mwa Khristu komanso mumzimu n'kukhala mtumiki wake wokhulupirika.[20]

Nditangoyamba kuwerenga Baibulo kwa nthawi yoyamba, ndinamva mphamvu ya Mulungu yomwe ija ndinamva ku ofesi ya ku Beverly Hills ija itadzadzanso mwa ine. Kenako Mulungu anandionetsanso masomphenya ena a Kumwamba ndi ku Gehena.[21] Ndinafuula kwa Mulungu kuti: "Ambuye, musanditumize ku Gehena!" Kenako ndinaona Kumwamba ndipo ndinamva mtendere wa Kumwamba.[22] Ngakhale kuti muuzimu ndinali wosaona, wamaliseche, komanso wamng'ono, ndinamuwuza Mulungu ndingasankhitsitse kukhalabe wosaona, wamaliseche, ndiopanda ntchito ngati atangondilola kumakhalabe ndi mtendere wa Kumwamba umenewu mpaka muyaya. Kenako ndinaonanso Gehena ndipo ndinakuwa kuti Mulungu andichitire chifundo komanso andikhululukire. Ndipo mphamvu ya Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera inalowa m'thupi langa.[23] Kudzera m'chikhulupiriro changa mwa Yesu ndi magazi ake amene anakhetsedwa chifukwa cha ine, ndiponso chifukwa cha chikhulupiriro changa, mawu a Mulungu amene ndinawamva ndi kuwatsatira,[24] ndinamva m'thupimu kuti tchimo lililonse limene ndinachitapo

**9** Mat. 13:39, chap. 24, 1 Akor. 15:24, Aheb. 9:26, 1 Pet. 4:7 **10** Aef. 2:1, 5, Akol. 2:13 **11** Ezek. 37:1

**12** Num. 24:16, 1 Sam. 2:3, Yobu 21:22, Sal. 32:8, Miy. 2:6, 3:20, 9:10, Luka 1:77, Aro. 11:33, 1 Akor. 1:25, 2:16, 3:19, 2 Akor. 4:6 **13** Sal. 44:21, 94:11, Yes. 46:9-10, 1 Akor. 3:20, 1 Yoh. 3:20, Chiv. 21:6, 22:13 **14** Gen. 35:5, Lev. 26:16, Yobu 31:23, Yer. 32:21, Ezek. 32:32, 2 Akor. 5:11 **15** Gen 1:1, Mal. 3:6, Mac. 4:24, 2 Akor. 5:11, Aheb. 13:8 **16** Sal. 5:11, 35:19, Yes. 51:11, 61:10, Yoh. 16:33, Mac. 2:28, 20:24, Aro. 12:8, 15:13, 2 Akor. 8:12 **17** Gen. 22:12, Sal. 112:1, Miy. 13:13, 14:16, 28:14, 31:30, Mlal. 7:18 **18** Miy. 8:36, Ezek. 18:2, 4, Chiv. 19:20, 20:10, 14, 15, 21:8 **19** Gen. 2:17, 6:7, 9, 13, Ex. 20:5, 32:33, 34:7, Ezek. 3:18, 18:20, Mat. 8:12, 22:13, Marko 16:16, Chiv. 2:5, 16, 22-23, 3:3, 20:15 **20** Yoh. 4:35-36, 15:5, 8, 15-16, Chiv. 14:18 **21** Yes. 5:14, 14:9, Luka 16:22-31, Mac. 7:55-56, Chiv. 4:1-11, 14:10-11, 15:1-4, 20:10, 21:2-5, 10-27, 22:1-5 **22** Aro. 5:1, Aef. 2:14, Afil. 4:7, Akol. 3:15, 1 Ates. 5:23, 2 Ates. 3:16 **23** Lev. 26:11-12, Yoh. 14:16, 2 Akor. 6:16, 1 Pet. 2:5, 1 Yoh. 3:24 **24** Hab. 2:4, Mat. 17:20, Luka 7:50, Mac. 20:21, 26:18, Aro. 1:17, 3:28, 5:2, 10:17, 11:20, Gal. 2:16, 3:11, Aef. 2:8, 3:17, Aheb. 10:38



***MAUTUMIKI A ALAMO PA INTANETI***
**www.alamoministries.com**

m'mbuyomu likuchoka.[25] Zitatero, ndinayamba kumva kuti ndine woyera.[26] Chinthu china chake chosangalatsa chinandichitikira, ndipo amene anandichitira chinthucho ndi Khristu Yesu, "Woyera wa Israeli."[27] Ndinasangalala kwambiri nditamasulidwa ku uchimo n'kulandira mphamvu imene imandithandiza kuti ndisamachimwe, ndipo ndikufunitsitsa kudziwitsa anthu onse padziko lapansi kuti nawonso amudziwe ndi kudzapeza moyo wosatha.

Ngakhale kuti ndakhala mu utumiki wa Khristu kuyambira mu 1964, ndikuonabe kuti umoyo wauzimu wochokera Kumwamba ukuyikidwa m'mafupa owuma aja nthawi iliyonse imene ndawerenga Baibulo. Mawu a Mulungu athandiza kuyikanso uwisi m'mafupa amene poyamba anali owuma, kuikamo minofu ndi khungu lomwe ndi chitetezo chauzimu. Mawu aliwonse a Mulungu athandiza Khristu alowe mumtima mwanga. Panopa ndikumvabe Mawu aliwonse a Mulungu amene analowa m'moyo mwanga kudzera mwa Mzimu Woyera. Mawu amenewa amandithandiza kukhala ndi mphamvu zozimitsira mivi yoyaka moto imene Satana wakhala akundiponyera pa zaka zonsezi. Ndikudziwa bwino kuti "ndife oposa ogonjetsa"[28] mwa Khristu Yesu, ndipo "timamudalira ndi mtima wonse."[29] Ndikudziwanso bwino kwambiri kufunika kotsatira Mawu aliwonse a Yesu, amene iye anawalankhula atatsala pang'ono kukwera Kumwamba mumtambo. Yesu ananena mawu akuti, "Pitani m'dziko lapansi, mukalalikire uthenga wabwino ku chilengedwe chonse."[30] (Kalalikireni kwa fupa lililonse lowuma, kutanthauza anthu amene ndi akufa mumzimu n'cholinga choti "amve Mawu a Ambuye."[31])

"Iye amene akhulupirira n'kubatizidwa adzapulumuka, koma iye amene sakhulupirira, adzawonongedwa."[32]

*(Yapitilira pa tsamba 8)*

**25** Marko 14:24, Yoh. 6:53, Mac. 20:28, Aro. 3:25, 5:9, Aef. 1:7, 2:13, Akol. 1:14, 20, Aheb. 9:12, 14, 22, 1 Pet. 1:18-19, Chiv. 1:5, 5:9 **26** Aheb. 10:19-22, 1 Yoh. 1:7, Chiv. 1:5, 7:14 **27** Sal. 89:18, Mac. 3:13-14 **28** Aro. 8:37, 1 Yoh. 4:3-4 **29** Akol. 2:10 **30** Marko 16:15, Luka 14:23 **31** 2 Maf. 20:16, Yes. 1:10, Yer. 2:4, Ezek. 37:4 **32** Marko 16:16, 2 Ates. 2:12



*M'busa wa Mgwirizano wa Tony Alamo Christian Ministries M.C. akugawira nkhani zimene Mbusa Alamo analemba—Democratic Republic of the Congo*

## Tanzania

Okondedwa Mbusa Alamo, mbusa wanga wokondeka komanso wotumidwa ndi Mulungu,

Chisomo, chifundo ndi mtendere zochokera kwa Atate ndi Khristu Yesu Ambuye wathu zikhale nanu komanso ndi utumiki wanu. Ndikuthokoza Mulungu, Amene ndakhala ndikumutumikira kuyambira mu 1994, ndipo ndine mtumiki ku Musoma, Tanzania. Ndakhala ndikuchita utumiki wanga m'dziko lonse la Tanzania komanso m'mayiko ena akunja kwa dziko la Tanzania. Abusa, n'zoona kuti ine sindinamvepo mawu anu ndipo sindinaonepo nkhope yanu, koma kudzera m'zimene mumalemba zomwe ndakhala ndikuwerenga, ngati nkhani yosangalatsa ndi yotsitsimula yakuti "Mafupa owuma," *Mesiya* ndi "Munda wa Mulungu," zomwe inuyo Mbusa Tony Alamo, mlaliki wamkulu padziko lonse munalemba. Kudzera m'nkhani zimenezi, ndafika podziwa ndiponso pomvetsa nkhawa imene muli nayo yokhudza tchalitchi, chomwe ndi thupi la Khristu. Ineyo pamodzi ndi anzanga amene ndimagwira nawo ntchito ya Ambuye komanso anthu amene angotembenuka kumene, omwe alandira Khristu kudzera m'nkhani zimene mumalemba, tapanga gulu lotchedwa Tchalitchi cha Gulu la Okhulupirira (Believer Community Church [B.C.C.]). Tikufunitsitsa kuti utumiki wanu ufalikire kudera la kum'mawa kwa Africa, makamaka ku Tanzania, ndipo tikufuna ufike makamaka kumadera a kumidzi. Chonde Abusa, tikufuna thandizo lanu. Tikupempha kuti mutitumizireko zinthu ngati masipika, jenereta, mabaibulo a anthu otembenuka mtima kumene komanso mabuku a nkhani zimene mumalemba n'cholinga choti tithandize anthu amene akungotembenuka kumene n'kulowa m'gulu lathu komanso kuti ntchito yathu iziyenda bwino. Mukachita zimenezi, Mulungu adzakudalitsani kwambiri. Tikupempha Ambuye kuti adalitse utumiki wanu komanso moyo wanu wauzimu chifukwa cha ntchito yabwino imene mukuchita. Ndife oyamikira, ndipo tikudikirira mwachidwi yankho lanu.

Ndine m'bale wanu mwa Khristu,

O.E.M. — Tanzania, East Africa

## California

Okondedwa Mbusa Alamo,

Ndikulemba kalatayi ndi mphamvu ya Mzimu Woyera, ndiponso nditavala zida zonse za nkhondo zochokera kwa Mulungu (Aefeso 6:10-17). Chaposachedwapa, kudzera mu kukula mu uzimu komanso kusonkhana ndi m'bale wa m'gulu la asilikali a Mulungu, zinsinsi zina za m'Baibulo zavumbulutsidwa ndi Mzimu Woyera. Ndikudziwa kuti panopa Mulungu akukonzekeretsa anthu Ake osankhidwa, ndipo ndinawerenga nkhani ina imene munalemba. Ndikukhulupirira kuti Mulungu wandithandiza kuti ndipeze nkhani zimene inuyo mumalemba pa nthawi yoyenerera pamene ndimafunika kudziwa mfundo zina zoona. Ndachita chidwi kwambiri ndi utumiki wanu. Ndaona kuti mukunena <u>zowona zenizeni</u>, osati mukungowuza anthu zinthu zotsekemera, zimene akufuna kumva ndiponso zowakomera m'khutu pankhani ya maulosi. Chonde, ndiyikeni pagulu la mamembala anu ndiponso ndikhale pagulu la anthu amene mumawatumizira nkhani zimene mumalemba n'cholinga choti ndikule mu Mzimu Woyera, nditanyamula lupanga la choonadi la Mulungu. Padakali pano ndili m'ndende, choncho musanditumizire mabuku koma nkhani zimene mwalemba pamapepala basi. Sindingathe kupereka ndalama iliyonse koma mapemphero oti gulu lanu la atumikili lipitirize kukula n'kukhala lamphamvu.

Ndine wanu,

B.L. — Corcoran, California

## INDIA

Moni ndi mafuno abwino kuchokera kwa abale anu a m'gulu la Tony Alamo Christian Ministries ku India.

Ndinasangalala komanso ndinayamikira kwambiri nditalandira Mabaibulo Opatulika komanso mabuku ndi nkhani zina zimene munalemba, monga zakuti, *Mesiya*. Mwapemphero, abale anga achikhristu pamodzi ndi ine tikugawira uthenga wopatsa chipulumutsowu kwa anthu amene amadziwa Chingelezi, komanso tikuyesetsa kumasulira uthengawu m'chinenero chathu chimene anthu ambiri omwe sadziwa Chingelezi amamva, ena mwa anthuwa amakhala m'madera a kumudzi. Anthu ambirimbiri, monga madalaivala a mabasi ndi magalimoto, ana a sukulu a kusekondale, a kuyunivesite, ogwira ntchito zolembedwa monga m'mafakitale, aphunzitsi, ndi ena onse, akuchita chidwi kwambiri ndi uthenga wachipulumutsowu. Anthu ambiri mumzinda wathu alandira Yesu Khristu kukhala Mpulumutsi wawo kudzera munkhani zimene mumalemba. Chonde, muzipempherera utumiki wathu m'mapemphero anu.

Ndine mtumiki wanu m'munda wa mphesa.

Ndatha ine,
Mbusa N.T. — Rampachodavaram Mandal, India



*Brother T.R. akugawa buku limene Mbusa Alamo analemba, Mesiya—Rajahmundry, India*

**Mawu otsatirawa analembedwa ndi Mbusa Alamo, m'buku lake lotchedwa, *Mesiya***

**Chozizwitsa Chichikulu Chimene Chinalembedwa:**

**Nkhani ya**

# Mesiya

### Mogwirizana ndi ulosi wa m'Baibulo

**"AMENEYU aneneri onse amchitira umboni" (Machitidwe10:43).**

**"Taonani, ndadza; M'buku mwalembedwa za Ine"**

**(Salmo 40:7, Ahebri 10:7).**

**(B) Yesaya 53** *(ikupitilira)*

**(9) Mesiya ANAZUNZIDWA KOOPSA, Yesaya 53:4-6, 8, 10-12:**

**"Zoonadi Iye ananyamula zowawa ZATHU, ndi kusenza zisoni ZATHU...Iye analasidwa chifukwa cha zolakwa ZATHU, natundudzidwa chifukwa cha mphulupulu ZATHU; chilango chotitengera IFE mtendere chinam'gwera Iye; ndipo ndi mikwingwirima yake IFE tachiritsidwa...Yehova anayika pa IYE mphulupulu ya ife tonse... Chifukwa cha kulakwa kwa ANTHU ANGA Iye anakhomedwa... Moyo wake ukapereka nsembe yopalamula." "Nadzanyamula mphulupulu ZAWO...Ananyamula machimo a ambiri."[1]**

**M'mutu umenewu mwafotokozedwa mazunzo oopsa amene Mesiya anakumana nawo.** M'mutuwu muli mavesi 12 okha, koma nthawi zokwana 14 mwatchulidwa mazunzo amene Yesu anafunika kukumana nawo kuti apereke nsembe yowombola anthu ku uchimo. Mugawo lonseli (Yesaya. 52:13-53:12) muli ulosi womwe tanthauzo lake linadziwika pamene Ambuye Yesu "änayesera...uchimo m'malo mwathu" (2 Akorinto 5:21) ndiponso pamene "anafera machimo athu" (1 Akorinto 15:3).

Yehova "anayika pa Iye mphulupulu ya ife tonse" (Yesaya 53:6). Mesiya ndiye anali Momboli amene anagweredwa ndi malawi onse a moto wolusa wa chiweruzo umene ukadakagwera pa munthu. Apatu Mulungu anasonyeza kuti ndi wachisomo kwambirit! Choncho, tingati Yesu anakhomedwa pamtanda mochititsa manyazi kwambiri, koma zimenezi zinathandiza kuti alandire ulemerero waukulu komanso zinathandiza kuti anthu apulumutsidwe. Pamene Ambuye Yesu anabwera, anakwaniritsa maulosi amenewa okhudza Mesiya komanso imfa Yake ya nsembe pa mtanda: "Amene anasenza machimo athu mwini yekha m'thupi mwake pamtanda" (1 Petro 2:24).

**(10) Mesiya adzavutika MWAKUFUNITSITSA ndipo sanadandaule, Yesaya 53:7:**

"Iye anaponderezedwa koma anadzichepetsa Yekha osatsegula pakamwa Pake; ngati nkhosa yotsogoleredwa kukaphedwa, ndi ngati mwana wa nkhosa amene ali du pamaso pa omsenga, motero sanatsegula pakamwa Pake."

Nthawi zambiri anthu akamazunzidwa amayamba kudandaula kapena kung'ung'udza, makamaka ngati munthu wina akuwachitira zinthu mopanda chilungamo. Koma Mesiya anachita zinthu zosiyana ndi zimenezi. Iye analolera kuti akumane ndi mavutowa n'cholinga choti "anyamule machimo athu" ngati nkhosa imene ikupita kukaphedwa. Mololera komanso mosanyinyirika, Mesiya anapilira nkhanza zowopsa, chifukwa zimenezi zinali chifuniro cha Yehova. Pamenepa tikutha kuwona chikondi chachikulu ndiponso chosatha chimene anatisonyeza.

M'Chipangano Chatsopano, pamene Yesu Khristu ankamenyedwa, kuyimbidwa mlandu wabodza, kuchitiridwa nkhanza, kunyozedwa,

**1** Olemba za Mulungu amalepheretsa kuti ukadaulo kapena phunziro lililonse lichotse chiphunzitso cha kufa kwa Yesu Khristu (vicarious atonement) kuchokera mu gawo ili pakulionetsa mowilikiza, m'maonekedwe osiyanasiyana koma lili lomwelo, kuti iye amene angakwanitse pa malo amodzi alimbikitsidwe kukumana nalo malo ena.




*Mbusa Mike Omoasegun ndi ena a mumpingo wake akulandira mabuku amene Mbusa Alamo analemba pamodzi ndi Baibulo la King James Version kuchokera ku Tony Alamo Christian Ministries—Suleja, Nigeria*

## Kuchokera pa lamya yathu ya pemphero ndi uthenga yomwe imagwira ntchito kwa maola 24

D.R. wa ku McAllister Library, Fuller Theological Seminary ku Pasadena, California, anaimba foni n'kunena kuti anapeza mapepala a nkhani zingapo zimene munalemba ndipo anaziwerenga. Iye akuti anasangalala nazo kwambiri ndipo wapempha kuti akhale pagulu la anthu amene amatumiziridwa nkhanizi nthawi zonse. Iye wapempha kuti azitumiziridwa nkhani iliyonse imene Mbusa Alamo walemba. Iye akufuna kuti akhale ndi nkhani zonse zimene Mbusa Alamo analemba n'cholinga choti anthu ofufuzafufuza azitha kubwera ku laibulale yake yosungira mabuku n'kumaphunzira Mawu a Mulungu a Mbusa Alamo. Iye anasangalala kwambiri ndi nkhanizi. Akuti akufuna zoti pashelefu yake ina padzadze mabuku a Mbusa Alamo okhaokha. Akuti Mbusa Alamo amanena zowona zokhazokha.

kulavuliridwa, kuzunzidwa, kukwapulidwa ndiponso kukhomedwa pamtanda, sanapse mtima kapena kukwiyira anthu amene ankamuzunzawo, koma anangopemphera.

Mboni zambirimbiri zitapereka umboni wabodza, mkulu wa ansembe anati, "Suvomera kanthu kodi?...Koma Yesu anangokhala chete" (Mateyu 26:59-63).

Ili ndi pemphero la Yesu limene anapemphera ali pamtanda: "Atate, akhululukireni, chifukwa sakudziwa chimene akuchita" (Luka 23:34).

Dongosolo lonseli ndilosayembekezereka, losagwirizana ndi chikhalidwe cha munthu, munthu sangachitire mwina koma kukong'onthedwa, kudzidzimutsidwa, ndi maulosi awiri onse makamaka pakukwaniritsa zimene zinanenedwa.

**(11) Atamutenga kuti akamuweruze, Mesiya adzakhala OPANDA MUNTHU OMUYIMILIRA kuchonderera kuti amumasule, ndipo sipadzapezeka munthu amene adzanene kuti Mesiyayo ndi wosalakwa, Yesaya 53:8:**

"Anachotsedwa ku chipsinjo ndi chiweruziro; ndipo ndani adzafotokoza nthawi ya moyo wake?"

Bwalo la Sanhedrin likamaweruza milandu yokhudza kupereka "chilango cha imfa," linkakonda kuyitana anthu amene amadziwapo kanthu pa nkhaniyo kuti adzapereke umboni wotsutsana ndi munthu amene akuyimbidwa mlanduyo. Izi sizinachitike pa mlandu wa Yesu wa ku Nazareti, koma zimene zinachitika ndi zakuti mlanduwo unaweruzidwa mwaphuma, mwachinyengo, komanso bwalo la Sanhedrin limeneli silinamve mbali zonse za mlanduwo. Choncho, mlanduwu umaweruzidwa mopanda chilungamo.

Oweruza a bwaloli omwe anali Ayuda achinyengo anaonetsetsa kuti Yesu akhale yekha popanda womuyikira umboni womuteteza. Oweruzawo analinso ndi mtumwi za ufumu wa Roma, womwe unali wamphamvu kwambiri pa nthawiyo. **Panalibe munthu ngakhale m'modzi amene anapereka umboni woteteza Yesu.** Yudasi anapereka Yesu; Petro anamukana mochita kulumbira; ndipo ophunzira ena onse "anamusiya iye, nathaŵa" (Mateyu 26:56). Ndipo azimayi ambiri amene pa nthawi ya utumiki Wake ankamutumikira, anayamba "kumuyang'anira patali" pa nthawi imene ankakhomedwa pamtanda (Mateyu 27:55). Pa nthawi imene tinganene kuti ankafunikira kwambiri thandizo, malinga n'kuona kwa anthu, PANALIBE MUNTHU NGAKHALE M'MODZI AMENE ANAIMA PAMBALI PAKE. Zowonadi, patapita nthawi, pambuyo pozunzidwa kwa maola ambiri, mayi ake Mariya pamodzi ndi azimayi ena ochepa omwe anali okhulupirika komanso mtumwi wake wokondeka Yohane, "anaima pambali pake" pamtanda. Koma nthawi yonse imene ankayimbidwa mlandu mpaka m'mbandakucha wa tsiku limene anaphedwa, anali yekhayekha, popanda aliyense. Pambiri yonse ya anthu, palibe munthu amene achibale ndi anzake anamuthawa ndi kumusiya yekhayekha ngati Yesu.

Yesu anamangidwa, OSATI ndi akuluakulu a boma koma ndi gulu lachiwawa. Baibulo limati: "Khamu

*(Yapitilira pa tsamba 6)*

## MESIYA

(Yachokera pa tsamba 5)

lalikulu la anthu, ndi malupanga ndi mikunkhu, kuchokera kwa ansembe aakulu ndi akulu a anthu" (Mateyu 26:47). Ngakhale Yesu weniweniyo ananena zoti anthuwa ankachita zinthu mopanda chilungamo komanso mokhala ngati sakudziwa chimene akufuna kuchita. Iye anati: "Kodi munatulukira kundigwira Ine ndi malupanga ndi mikunkhu, ngati wachifwamba? Tsiku ndi tsiku ndimakhala m'Kachisi kuphunzitsa, ndipo simunandigwira. Koma izi zonse zinachitidwa, kuti zolembedwa za aneneri zikwaniritsidwe" (Mateyu 26:55-56).

Kenako mboni ZONYENGA zinayitanidwa kuti zipereke umboni wonama ndi cholinga chakuti "amuphe Iye" (Mateyu 26:59), ndipo anazengedwa mlandu usiku, zomwe zinali zosemphana ndi malamulo.

Pamene anali kukhoti la Chiroma, Pilato anayesetsa kumupezera chifukwa choti amuphere koma analephera, ndipo anafunsa anthu kuti, "anachita choipa chotani?" Mayankho omwe anamva anali opanda nzeru ochokera kuchikhamu cha anthucho, ndipo atsogoleri awo ankati, "Apachikidwe pamtanda... Apachikidwe pamtanda" (Mateyu 27:22-23). Kenako Pilato ataona kuti sizitheka kupulumutsa Yesu ndiponso kuti anthuwo ankapitirizabe "kufuwula," anagonja n'kulolera zofuna za anthuwo. Iye anangowasambira m'manja n'kumupereka Yesu kwa iwo kuti akamupachike (Mateyu 27:22-26). Apatu Yesu anaweruzidwa mopanda chilungamo ngakhale pang'ono.

Koma si Pilato yekha amene anawona kuti Khristu anali wosalakwa pamene ananena kuti "ine sindipeza chifukwa mwa Iye" (Yohane 19:6)—winanso anali m'neneri wakale amene analosera za Mesiya kuti: "Iye sanachita chiwawa, ndipo m'kamwa mwake munalibe chinyengo" (Yesaya 53:9).

*Yapitilira mu nkhani zammakalata vol 06100*

## Zambia

Wokondeka Mbusa Tony Alamo,

Ndine wokondwa kukulemberani kalata. Kodi muli bwanji inu Abusa? Ndikukhulupirira kuti mwachisomo cha Mulungu Wamphamvu yonse, muli bwino. Ndinawerenga nkhani yomwe munalemba yakuti "Atsogoleri Ndiponso Nthano," ndipo Mulungu anandilola kuti ndipeze nkhani imeneyi m'njira yodabwitsa kwambiri. Nditawerenga nkhaniyi, ndinadalitsika kwambiri ndipo ndinakhala ndi mtima woti ndikulembereni kalata. Ndikukuthokozani chifukwa cha uthenga wotsitsimutsa wopita kwa anthu otayika komanso amene sanapulumutsidwe n'cholinga choti amulandire Khristu m'mitima yawo. Kudzera m'mabuku ndi nkhani zimene mumalemba, anthu ambiri adziwa Khristu ndipo apulumutsidwa kwa mdyerekezi. Mulungu akudalitseni ndi chuma, thanzi labwino, komanso akudalitseni mu uzimu.

Abusa, ndine mayi wachitsikana ndipo ndinalowa m'banja zaka zisanu zapitazo. Ndinapereka moyo wanga kwa Yesu zaka ziwiri zapitazo, ndipo Ambuye wakhala akundikomera mtima. Ndikufunitsitsa kulalikira uthenga wabwino wonena za Yesu kwa anthu ena. Monga m'mene zilili ndi amayi ambiri ku Africa kuno, ndakhala ndili mu ukapolo kwa nthawi yayitali chifukwa cha miyambo ndi zikhulupiriro, choncho ndikufunitsitsa kupereka moyo wanga kwa Ambuye. Abusa, ndikupempha kuti munditumizireko maBaibulo, mabuku, nkhani zimene mumalemba, uthenga wa Mulungu pa matepi, komanso zinthu zina zimene ndingathandizire anthu osochera. Pomaliza, ndikupempha kuti munditumizire mabuku ophunzirira Baibulo komanso matepi a nyimbo.

Ndine m'bale wanu mwa Khristu,
L.M.
Isoka, Zambia

---

Wokondedwa Mbusa Tony Alamo,

Ndine wosangalala kukupatsani moni m'dzina la Ambuye wathu Yesu Khristu. Ndikuyamika Mulungu chifukwa cha moyo wanu komanso m'mene Iye anakonzera zoti azikugwiritsani ntchito pofalitsa Mawu ake n'cholinga choti anthu a m'madera osiyanasiyana padziko lonse lapansi apulumutsidwe. Mbusa Alamo, ineyo poyamba ndinali munthu wosapemphera koma amene anandithandiza kuti ndisinthe ndi mnzanga amene ndimagwira naye ntchito, ndipo kenako nditawerenga uthenga wanu munkhani zimene mumalemba, mtima wanga unatseguka, ndipo ndikukhulupirira kuti Mulungu akusintha moyo wanga. Ndinazindikira zoti Mulungu akufuna zoti tikhale achilungamo ngati Iyeyo. Mbusa Alamo, ndikupempha kuti munditumizire Baibulo limodzi kapena awiri a Chingelezi n'cholinga choti mnzanga nayenso aziwerenga Mawu a Mulungu Wamphamvu yonse. Mtendere wa Ambuye wathu ukhale nanu mu mzimu. Ndikukuthokozani kwambiri chifukwa cha kukoma mtima kwanu komanso poyankha mauthenga athu molimbikitsa.

Zikomo.
G.N. Kitwe, Zambia

## Mexico

Wokondedwa Mbusa Alamo,

Mabuku anu, omwe ali ndi uthenga komanso umboni wosangalatsa, afika paliponse ngakhale kudera limene ineyo ndikukhala. N'zosakayikitsa kuti Mulungu akukugwiritsani ntchito kwambiri kuti uthenga wake wachipulumutso ufike kwa munthu aliyense. Ineyo ndakhala ndili m'ndende kwa zaka 7 ndi hafu pa mulandu wozembetsa chamba. Pa zaka ziwiri zapitazi, Mulungu anandionekera m'njira yodabwitsa kwambiri. Ndikukhulupirira kuti nditulutsidwa chaka chino ndipo ndikufuna kupempha ngati munganditumizire buku lanu lakuti *Mesiya* pamodzi ndi mabuku ena amene ndingagwiritse ntchito pophunzitsa ana anga.

M.A. Monclova, Coahuila, Mexico

# Utumiki wa Alamo pa intaneti

## Ghana

Wokondedwa Abusa,

Ndine wosangalala kwambiri chifukwa munanditumizira nkhani zimene mumalemba. Ndalandira mtokoma wa nkhani zanu mlungu wathawu. Wokondedwa mtumiki wa Ambuye, anthu anasangalala kuwerenga nkhani zimenezi. Anzathu amene ali m'midzi, amene takhala tikuchita nawo mapemphero, anawerenga nkhanizi mosangalala kwambiri ndipo moyo wa anthu angapo wasintha chifukwa chowerenga nkhani zimenezi. Tidzasangalala kwambiri ngati mungatiyike pagulu la anthu amene nthawi zonse mumawatumizira nkhani za uthenga wabwino zimene mumalemba. Tikufunikira maBaibulo, mabuku anu, komanso ziphunzitso zanu.

Tikukupempherererani pamodzi ndi mwana wanu wokondedwa, Sion, komanso anthu onse amene akugwira ntchito pamodzi ndi inu. Mulungu akudalitseni. Komanso kukupemphani kuti muzitipempherera chifukwa pemphero limachititsa kuti dzanja la mphamvu la Mulungu Wamphamvu yonse ligwire ntchito. Popanda pemphero, ndiye kuti "tingagwire ntchito pachabe." Chonde, tikukupemphani kuti muzipemphereranso anzathu amene amadzipereka kupita kumidzi yakutali komanso kumadera a mapiri kukagwira ntchito ya Ambuye. Muziwapempherera kuti apitirize kukhala olimba mtima, achikhulupiriro komanso achikondi. Pemphero lathu ndi lakuti Mzimu wa Ambuye ukhale mtsogoleri wanu. Mulungu akudalitseni kwambiri kuti mukhale ndi moyo wautali, mtendere ndiponso zinthu zizikuyenderani bwino.

Timakukondani mwa Khristu,
A.S. Accra, Ghana

---

Wokondeka Mbusa Tony,

Zikomo ponditumizira buku lakuti *Mesiya* pamodzi ndi nkhani zokwana 10 zimene munalemba. Zimenezi zandithandiza kuti ndimudziwe bwino Mulungu ndiponso ndizimutumikira mwakhama kwambiri. Zina mwa nkhanizi ndinazipereka kwa anzanga ena achikhristu amene anafowoka muchikhulupiriro. Nditawayendera patapita nthawi, onse anasonyeza kuyamikira kwambiri ndipo ayambiranso kutumikira Mulungu mwachangu. Anthu amenewa ali ndi njala yofuna nkhani zinanso zimene munalemba. Choncho, ndikupempha kuti mutumize nkhani pafupifupi 150 komanso maBaibulo n'cholinga choti anthu ena amene angotembenuka kumene azigwiritsa ntchito. Ndiyamikira kwambiri mukanditumizira zinthu zimenezi. Ndikuthokoza zedi chifukwa cha ziphunzitso za Mawu a Mulungu zimene mwakhala mukuzipereka mokhulupirika kwa nthawi yaitali. Mulungu akudalitseni ndi chikhulupiriro chimene mungasunthe nacho mapiri.

Ndine mwana wanu mwa Khristu,
T.O. Kumasi, Ghana

## Nigeria

Wokondedwa Abusa,

Landilani moni m'dzina la Ambuye Yesu Khristu. Ame. Ndagawira nkhani zonse zimene munanditumizira chaposachedwa, ndipo ndasangalala kwambiri nditaona m'mene anthu omwe awerenga nkhanizi asinthira miyoyo yawo. Anthuwa akulonjeza kuti ayamba kutumikira Ambuye ndi mtima wawo wonse, ndipo ena akuti akulemberani kalata. Ndikupempha kuti munditumizire makope 25 a buku la mutu wakuti *Mesiya* ndiponso mapepala 150 a nkhani zosiyanasiyana zimene munalemba. Mungatumizenso maBaibulo, ndi mabuku ena amene angathandize pa ntchito yolalikira za Ambuye Yesu Khristu ngati tingawagawire kwa achibale, anzathu komanso anthu ena amene angafune. Ndikufunitsitsa nditakhala m'gulu la anthu a gulu lanu amene akugwira ntchitoyo kuno ku Nigeria. Chonde, ndiuzeni zoyenera kuchita kuti zimene ndikufunazi zitheke. Ndaona kuti dzanja la Mulungu lili ndi inu ndipo ndikufuna kuti nanenso ndizichita nawo utumikiwu. Ndikuyembekezera mwachidwi yankho lanu.

Ndine wanu mwa Ambuye,
R.M.
Port Harcourt, Nigeria

## Togo

Wokondedwa mwa Khristu,

Ndife osangalala polandira kalata yanu komanso mabuku amene munatitumizira. Mulungu akutithandizadi. Anthu pafupifupi 15 tsopano adziwa Khristu kudzera m'mabuku anu ndipo ndikupemphera kuti Mulungu akudalitseni nonse.

Komabe, tikufunikirabe maCD ndi maBaibulo ambiri. Koma patokha sitingakwanitse kugula zinthu zimenezi chifukwa dziko lathu la Togo ndi losawuka kwambiri.

Tikukhulupirira kuti mutitumizira maCD ndi maBaibulo pa nyengo ya pasikayi.

Madalitso akhale nanu m'dzina la Yesu. Ameni.
Mbusa Henry James
Lome, Togo

---

Wokondedwa Abusa,

Landirani moni wochokera kuno ku Ghana. Nditawerenga buku lanu lakuti *Mesiya,* tsopano ndine wokondwa kukudziwitsani kuti ndalandira Yesu Khristu kukhala Mpulumutsi wanga komanso zoti iye anandifera. Poyamba sindikadziwa Mulungu ngakhalenso Mwana wake, Mesiya. Koma nditawerenga bukuli, ndizindikira kuti ndinali mumdima koma Ambuye wandionetsa kuwala. Panopa ndine Mkhristu wobadwanso ndiponso mwana wa Mulungu wamoyo. Padakali pano ndilibe Baibulo. Choncho ngati n'kotheka, munditumizireko pamodzi ndi buku lakuti *Mesiya*. Ndiyamikiranso ngati munganditumizire buku lililonse limene linganditandize kumudziwa bwino Mulungu. Panopa ndimapita kutchalitchi cha Pentekosite ku Koforidua. Ambuye Mulungu akudalitseni kwambiri.

Ndine,
D.F. Koforidua, Ghana

## UMBONI WA TONY ALAMO

*(Yachokera pa tsamba 3)*

Ngati inuyo muli ngati ine ndipo simukufuna kudzawonongedwa, koma mukufuna kudzapulumuka, nenani pemphero ili kwa Mulungu:

**AMBUYE wanga komanso MULUNGU wanga, ndichitireni chifundo ndine munthu wochimwa.[33] Ndikukhulupirira kuti YESU KHRISTU ndi MWANA wa MULUNGU wamoyo.[34] Ndimakhulupiriranso kuti IYE anafera pamtanda ndipo anakhetsa mwazi WAKE wamtengo wapatali ndi cholinga choti machimo anga onse akhululukidwe.[35] Ndikukhulupiriranso kuti MULUNGU anaukitsa YESU kwa akufa pogwiritsa ntchito mphamvu ya MZIMU WOYERA,[36] ndiponso kuti IYE anakhala kudzanja lamanja la MULUNGU ndipo panopa akumva pemphero langa lolapali.[37] Ndikutsegula zitseko za mtima wanga, ndipo ndikukuyitanani kuti mulowe mumtima mwanga, inu AMBUYE YESU.[38] Tsukani machimo anga ambirimbiri achoke onse mu mwazi wamtengo wapatali umene INU munakhetsa m'malo mwanga pamtanda wa ku Kavari.[39] Ndikudziwa kuti mundimvera pemphero langali AMBUYE YESU; INU mukhululukira machimo anga ndi kupulumutsa moyo wanga. Ndikudziwa izi chifukwa MAWU ANU, Baibulo, limanena zimenezi.[40] MAWU ANU amati INUYO simudzakana kumvetsera pemphero la munthu aliyense, ndipo ine ndili m'gulu la anthu amenewo.[41] Choncho, ndikudziwa kuti INUYO mukundimvetsera pamene ndikupemphera ndipo ndikudziwanso kuti INUYO mundiyankha komanso mundipulumutsa.[42] Ndipo ndikukuthokozani AMBUYE YESU, chifukwa chopulumutsa moyo wanga, ndipo ndisonyeza kuyamikira mwa kuchita zinthu zimene INUYO munalamula komanso kupewa kuchita uchimo.[43]**

Pambuyo pa chipulumutso, YESU ananena kuti munthu ayenera kubatizidwa pomizidwa thupi lonse m'madzi, m'dzina la ATATE, ndi la MWANA, ndi la MZIMU WOYERA.[44] Muziphunzira mwakhama Baibulo la *Buku Lopatulika Ndilo Mau a Mulungu*, [King James Version] ndipo muzichita zimene Baibulolo limanena.[45]

AMBUYE akufuna kuti inuyo muziwuza ena za chipulumutso chanu. Mungathe kukhala wofalitsa uthenga wabwino wa Mbusa Tony Alamo. Tizikutumizirani mabuku mwaulere. Imbani foni kapena tumizani imelo kwa ife kuti mudziwe zambiri. Tikukupemphani kuti muwuzeko ena uthengawu.

Ngati mukufuna kuti dziko lipulumutsidwe monga m'mene YESU akulamulira, mukufunika kupereka chakhumi kwa MULUNGU. MULUNGU anati, "Kodi munthu angabere MULUNGU? Inde, mwandibera kale. Koma akuti, Ife tikumubera bwanji MULUNGU? Mu chakhumi ndi mu zopereka. Anthuwo ndi otembereredwa chifukwa akundibera, ngakhale mtundu wonsewu [dziko lonse lapansi]. Bweretsani nonse chakhumi ['chakhumi' ndi gawo limodzi la magawo khumi (10%) ya malipiro anu] m'nkhokwe zanga n'cholinga choti pakhale nyama [chakudya cha Uzimu] mu nyumba YANGA [anthu opulumutsidwa] kuti mundiyese, akutero AMBUYE wa MAKAMU, kuti muone ngati sindidzakutsegulirani mazenera a Kumwamba ndi kukukhuthulirani madalitso amene mudzasowa malo owalandirira." Ndipo ndidzadzudzula anthu okudyerani masuku pamutu ndipo sadzawononga zipatso za nthaka yanu; ngakhalenso mphesa wanu sudzalephera kubala zipatso pa nyengo yake m'minda yanu, watero AMBUYE wa MAKAMU. Ndipo mitundu yonse idzakutchani odala: chifukwa dziko lanu lidzakhala labwino, watero AMBUYE wa MAKAMU" (Malaki 3:8-12).

---

**33** Sal. 51:5, Aro. 3:10-12, 23 **34** Mat. 26:63-64, 27:54, Luka 1:30-33, Yoh. 9:35-37, Aro. 1:3-4 **35** Mac. 4:12, 20:28, Aro. 3:25, 1 Yoh. 1:7, Chiv. 5:9 **36** Sal. 16:9-10, Mat. 28:5-7, Marko 16:9, 12, 14, Yoh. 2:19, 21, 10:17-18, 11:25, Mac. 2:24, 3:15, Aro. 8:11, 1 Akor. 15:3-7 **37** Luka 22:69, Mac. 2:25-36, Aheb. 10:12-13 **38** 1 Akor. 3:16, Chiv. 3:20 **39** Aef. 2:13-22, Aheb. 9:22, 13:12, 20-21, 1 Yoh. 1:7, Chiv. 1:5, 7:14 **40** Mat. 26:28, Mac. 2:21, 4:12, Aef. 1:7, Akol. 1:14 **41** Mat. 21:22, Yoh. 6:35, 37-40, Aro. 10:13 **42** Aheb. 11:6 **43** Yoh. 5:14, 8:11, Aro. 6:4, 1 Akor. 15:10, Chiv. 7:14, 22:14 **44** Mat. 28:18-20, Yoh. 3:5, Mac. 2:38, 19:3-5 **45** Deut. 4:29, 13:4, 26:16, Yos. 1:8, 22:5, 2 Tim. 2:15, 3:14-17, Yak. 1:22-25, Chiv. 3:18

*Ngati mukufuna kudziwa zambiri kapena ngati mukufuna mabuku kapenanso nkhani zina zimene zimakusangalatsani, tiimbireni foni kapena tilembereni.*

**Tony Alamo, World Pastor, Tony Alamo Christian Ministries Worldwide • P.O. Box 2948, Hollywood, CA 90078**

**Twenty-four hour prayer and information line: (661) 252-5686 • Fax (661) 252-4362**

**www.alamoministries.com • info@alamoministries.com**

*Tony Alamo Christian Ministries Worldwide imalandira anthu onse ndipo imapereka zinthu zofunika Kwa onse amene ali ku U.S. amene akufunitsitsadi kuti ayambe kutumikira AMBUYE ndi mtima wawo wonse moyo wawo wonse ndi mphamvu zawo zonse*

**Maservice amachitikira ku New York City lachiwiri lililonse nthawi ya 8 koloko usiku ndi malo ena usiku okhaokha.**

**Chonde imbani (908) 937-5723 kuti mudziwe zambiri. ZAKUDYA ZIMAGAWIDWA PAMAPETO PA MAPEMPHERO ALIWONSE.**

**Funsani buku la M'busa Alamo, lakuti *Mesiya,* losonyeza KHRISTU kuyambira ku Chipangano Chakale mu maulosi oposa 333.**

*Khalani wogwira ntchito yokolola miyoyo ya anthu pakukhala ogawira mabuku a M'busa Alamo*

*Mabuku ndi zinthu zonse zomvetsera n'zaulere, ndipo simulipira ndalama yotumizira*

*Ngati wina akukuuzani kuti mupereke ndalama pa zinthu zimenezi, chonde imbani pa (661) 252-5686.*

**M'BUKU ILI MULI CHIKONZERO CHENICHENI CHA CHIPULUMUTSO (Machitidwe 4:12).**

**MUSALITAYE, PATSANI ENA KUTI AWERENGE.**

**Anthu amene muli m'mayiko ena, tikukulimbikitsani kuti mumasulire n'chinenero chanu mabukuwa. Ngati mukusindikizanso bukuli, musaiwale kuika mawu ali m'munsiwa omwe ndi okhudzana ndi zamalamulo:**

© Copyright November 1995, March 2012, 2014 All rights reserved World Pastor Tony Alamo ® Registered November 1995, March 2012, 2014

CHICHEWA/NYANJA—Vol. 06000—*Tony Alamo's Testimony—Dry Bones*